*Baptist Publishing House*
OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O.BOX 1995 LUSAKA

7105



# Malamulo Khumi ndi Mkristu Lelo

W122
Nyanja

THE TEN COMMANDMENTS AND THE CHRISTIAN TODAY
(Nyanja)

First Published in Zambia
July 1, 1974
The Baptist Publishing House of
the Baptist Mission of Zambia
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

BWERANI AZIMAI

Bwerani Azimai
Konse lalikani
Muyimbeni
Kristu ndiye M'lungu
Kristu anauka
Kristu ndiye nyali
Tamandani

Bwerani ana onse
Ndi alongo onse
Phunzitsani
Kuli wodwala
Akufokafoka
Akukhala mdima
Pempherani.

Gwirani nchito zanu
Limbikani ndi mphamvu
Mupatseni
Cikondano canu
M'tima idzakondwa
Ndi cikondi cace
Tiyembekeze.

Ngati tidzazituta
Mulungu atipatsa
Muzambiri
Kristu wofatsa
Onse adzamfuna
Alimphoto yathu
Ndi cotsata.

7105

ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. Ndipo laciwiri lolingana nalo ndi ili, Uzikonda m'nzako monga udzikonda iwe mwini. Pamalamulo awa awiri mpokolowekapo cilamulo conse ndi aneneri. Mateyu 22:37-40)

Ngati tikonda Mulungu ndi mitima yathu yonse miyoyo yathu yonse ndiponso nzeru zathu zonse, tidzakondanso anansi athu monga momwe tidzikondera ife eni ace. Pamenepo cidzakhala capafupi kutsunga malamulo a Mulungu amene Mulungu adatipatsa.

PEMPHERO: Pempherani kuti tidzakhala ndi cikondi pa Mulungu ndi pa anthu ena. Pempherani kuti Mulungu akhale woyamba pa miyoyo yathu.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9.

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:17 |
| Laciwiri | 1 Mafumu 21:5-6 |
| Lacitatu | 2 Samueli 11:2-3 |
| Lacinai | Mateyu 6:19-21 |
| Lacisanu | Luka 12:20-21 |
| Loweluka | Luka 12:15 |
| Lasabata | Akolose 3:5 |

Njila yabwino nimoyo ndi kupasa, osati kutenga. Tiyenela kufunsa Mulungu kuti acotse kusirira konse m'miyoyo yathu.

GAWO LACINAI: Tonse tili ndi zifuno zambiri. Nanga tingazitetedze bwanji ku ucimo wa cisiriro?

Cinthu cimodzi cimene tingacite ndi kukana kuika maganizo pa zinthu zimene ndi zolesedwa. Musayanganitsise cinthu cimene mudziwa kuti simungacipedze.

Cinthu cina cimene tingacite ndi kuzipeleka kwa Yesu Kristu. Ngati Kristu ali woyamba m'miyoyo yathu, zinthu za padziko lapansi sidzikhalanso zofunika.

Kusirira ndi ucimo wa m'mtima. Ubwela ndi cifuno cofuna kuti zinthu zonse zikhale zako. Mulungu afuna kulamulila miyoyo yathu yanthunthu angakhale maganizo athu ndi zifuno za m'mitima yathu. Cifuno cofuna kuti zinthu zonse zikhale zako cikula m'mutima m'mene mulibe cikondi. Tiudzidwa mu Buku Lopatulika kuti tidzikonda anansi athu monga momwe tizikonda efe eni. (Mateyu 22:39.)

Cikondi coona pa anthu ena cidzatiletsa kucita ma ucimo ambiri. Cikondi coona pa anthu ena cidzatiletsa kusirira. Ngati tiona m'mene tinga pasire anthu ena ndi m'mene tingathandizire anthu ena, tidzaona kuti palibe nthawi pokhalira ndi cifuno coti zinthu zonse zikhale zathu.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Pa miyezi itatuyi taphunzira malamulo onse khumi. Ndi cofunika kuti tisunga malamulo a Mulungu.

Yesu anafunsidwa za malamulo. Adati, "...Ndipo Yesu anati kwaiye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili

koposa kutumikira Mulungu. Sitidzakhala ndi mipingo yolimba kufikira akristu afunadi kutumikira Mulungu koposa cinthu cina ciri conse. Akristu ayenela kuika Mulungu poyamba, angakhale ndalama zao ziyenela kubwela pambuyo. Ngati tipitilidza kum'bera Mulungu cikhumi cace mipingo yathu siidzakhala yolimba. Akristu adzapitilira kukhala ofoka cifukwa mitima yao ili pa cuma cao.

Mulungu anati kwa munthu wina amene adakonda ndalama ndi zinthu zimene anali nazo koposa Mulungu "..Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako; ndipo zinthu zimene unazikonza zidzakhala za yani? Atero iye wakudziunjikira cuma mwini yekha wosakhala naco cuma ca kwa Mulungu!" (Luka 12:20, 21).

GAWO LACITATU: Lero anthu ambiri afuna kutenga zinthu osapeleka kanthu kina. Iyi ndi njira ina yopwanyira lamulo la Mulungu, "Usasirire." Kodi cifukwa ninji anthu atsewera njuga? Cifukwa cakuti ali ndi cifuno cofuna kupedza zinthu pamene iwo sapelekapo kanthu.

Pa njuga anthu ambiri amabwela ndi ndalama zao zimene zifunidwa ndi mabanja ao kuti akagule zakudya ndi zobvala. Ana amataya ndalama ku lotale pamene azimai a kunyumba kwao ndi ana ao ali osowa zinthu zambiri. Onse akufuna kupedza zinthu pamene iwo sanapelekepo kanthu.

Kutsewera njuga sikwabwino. Ndi njira yoipa yotaila ndalama. Mulungu sakondwera ndi zimenezi.

Yesu adati "...Yang'anirani, mudzisungire kupewa msiriro uli wonse: cifukwa moyo wace wa munthu sulingana ndi kucuruka kwa zinthu zace ali nazo." (Luka 12:15). Paulo adati kusirira ndi kupembedza mafano (Akolose 3:5). Ici ciri tere cifukwa munthu amene atsirira aika zinthu ndi zilako-lako zace kukhala zopambana Mulungu pa moyo wace. Dzinthu zimene afuna kwambiri zikhala fano kwa iye.



## ZA M'KATIMU


| PROGRAMU | | TSAMBA |
|---|---|---|
| 1 | MULUNGU AYEMBEKEDZERA ULEMU NDI KUMVERA | 1 |
| 2 | OSATI MILUNGU INA | 5 |
| 3 | KUPEMBEDZA KOONA KWA MULUNGU WOONA | 9 |
| 4 | KULEMEKEDZA DZINA LA MULUNGU | 14 |
| 5 | KUTSUNGA TSIKU LA AMBUYE | 18 |
| 6 | KULEMEKEDZA MAKOLO | 23 |
| 7 | KULEMEKEDZEDWA KWA MOYO WA MUNTHU | 28 |
| 8 | KUFUNIKA KOKHALA WOSADETSEDWA | 33 |
| 9 | USABE | 38 |
| 10 | KULANKHULA BWINO | 43 |
| 11 | KUFUNA ZINTHU ZOIPA | 48 |

Naboti. Maboza a mboni zonama anakhulupirira ndipo Naboti anaponyedwa miyala kufikira anamwalira. Pambuyo pace mfumu Ahabu adatenga munda wa mphesawo.

Ucimo wa Davide wa cigololo unayamba ndi cisiriro. Davide anayangana Bathsheba, amene adali mkazi wa mwini. Anafuna kuti amukwatire. Cifuno coipaci m'mtima wace cinali cacikulu kwambiri kuti cinamupangitsa Davide kuti acite cigololo. Pofuna kubisa ucimo wace, Davide adatuma mwamuna wa Bethsheba ku nkhondo kuti akaphedwe. (Nthano ili mu 2 Samueli 11:1-27.)

Mau acimo amenewa akuba, kunama, kupha ndi zigololo onse anayamba ndi cifuno coipa m'mtima pa cinthu cimene cinali ca mwini. Kusirira m'mtima kupititsa ku macimo ena oipa. Ici ndiye cifukwa cace sitiyenera kusirira zinthu zimene ziri za eni ace.

**GAWO LACIWIRI:** Kufuna koposa zimene munthu afuna, koposa zimene munthu angagwiritse nchito, ndi kusirira. Lero anthu akufuna zinthu zambiri-mbiri. Sikulakwa kufuna kukhala ndi zinthu. Koma ndi kulakwa kuti munthu nthawi zonse aziganizira cabe zofuna kukhala ndi zinthu.

Anthu ambiri lero akufunitsitsa zinthu za padziko pano koposa zinthu za Uzimu. Yesu adati, "Musadzikundikire nokha cuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi dzimbiri ziononga; ndi pamene mbala ziboola ndi kuba: Koma mudzikundikire nokha cuma m'mwamba, pamene njenjete kapena dzambiri sizionongа, ndipo mbala siziboola ndi kuba; pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso." (Mateyu 6:19-21).

Akristu ambiri m'machalichi athu ali ndi ndalama mu mabanki ao, koma akana kupeleka cikhumi cakwa Mulungu. Ici ndi cifukwa cakuti mitima yao yifuna kukhala cabe ndi ndalama

PROGRAMU 11

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KUFUNA ZINTHU ZOIPA.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"Usasirire nyumba yace ya m'nzako, usasirire mkazi wace wa m'nzako, kapena wanchito wace wa mwamuna, kapena wanchito wace wa mkazi, kapena ng'ombe yace, kapena buru wace, kapena kanthu Kali konse ka m'nzako."*

*Eksodo 20:17*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Mau a Mulungu atiudza kuti tisasirire cinthu ca mwini. Kusirira ndi kufuna cinthu ca mwini kuti cikhale cako.

Malamulo ena aletsa zinthu zina zochulidwa kuti zisacitike. Lamuloli liletsa cifuno cocitira ucimo. Kusirira ndi cifuno ca m'mtima cofuna kuti zinthu zonse zikhale zako. Cifunoci cicokela mukutsirira ndi muumbombo. Munthu amene asirira zinthu zimene sidzingakhale zace aonetsa kucepa kwa cikhulupiriro cace mwa Mulungu.

Lero tidzaphunzira zimene Mulungu anena za ucimowu.wa kusirira.

GAWO LOYAMBA: Kusirira kumodzi kuoneka pamene tifuna cinthu cimene sicathu. Sitiyenera kusirira zinthu za m'nansi wathu kuti zikhale zathu, kapena nyama zace, anchito ace, angakhale mkazi wace.

M'cipangano cakale tiuzidwa za mfumu Ahabu. (Nthanoyi ili mu 1 Mafumu 21). Ahabu anali kufuna munda wamphesa umene Naboti anali nawo. Naboti anakana kugulitsa mundawo kwa mfumu. Kusirira kunazaza mtima wa Ahabu. Anakana kudya. Pambuyo pace Yezebeli, mkazi wa mfumu, anakonda kuti mboni zonama zimupatse mlandu



PROGRAMU 1

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: **MULUNGU** AYEMBEKEDZERA ULEMU NDI KUMVERA.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"...Ngati mudzamvera mau anga ndithu, ndi kusunga cipangano canga, ndidzakuyesani cuma canga ca padera koposa mitundu yonce ya anthu."*

*Eksodo 19:5*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Lero tidzayamba maphunziro a malamulo khumi. Malamulowa anapatsidwa ndi Mulungu kwa anthu ace pa nthawi ya cipangano cakale. Anali malamulo okhalira moyo wolungama.

Malamulo khumi akali malamulo a Mulungu kwa ife. Lero tidzaphunzira tanthaudzo la malamulo khumi kwa akristu m'matsiku ano a 1974.

Ndidzawelenga malamulo khumi kucokera mu Buku Lopatulika. Akupedzeka mu Eksodo 20:1-17.

(Welengani mu Buku lanu Lopatulika Eksodo 20:1-17.)

GAWO LOYAMBA: Mulungu adatulutsa ana a Israyeli mu ukapolo mu Aigupto. Adati, "Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene ndinaturutsa iwe ku dziko la Aigupto, ku nyumba ya ukapolo." Eksodo 20:2.

Mulungu adali kuwaudza kuti tsopano sanalinso akapolo ai koma anali anthu a mtendere, omatsuka. Tsopano ndi Mulungu cabe amene adali mfumu yao. Ankayenela kumukonda ndi kumutunukira ndi kucita zinthu monga ana ace.

Malamulo khumi ananetsa zimene Mulungu anali kuyembekedzera kwa iwo.

Tidziwa kuti kutsunga malamulo khumi sikutipanga ife kukhala akristu. Sitingakhale abwino kwambiri kuti tidzapulumusidwe. Sitingapulumusidwe ndi kanthu kali konse kamene tingacite ife tokha. Tipulumutsidwa ndi cikhulupiriro mwa Yesu Kristu.

"Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu, ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera ku nchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense." Aefeso 2:8, 9. Pamene tilapa macimo athu ndi kulandira Yesu Kristu monga mpulumutsi wathu, timakhala ana a Mulungu. Tipulumutsidwa tsopano ndi kumoyo wosatha.

Titapulumutsidwa, tiomboledwa ku ukapolo wa ucimo. Mulungu amakhala Ambuye athu. Amafuna kuti tidzimukonda ndi kumutumikira ndi kucita zinthu monga ana. Malamulo khumi akali kutionetsa ife zimene Mulungu ayembekedzera kwa ife. Ngati timulola kuti atero, adzatipatsa mphamvu yoti tisunge malamulo ace.

GAWO LACIWIRI: Buku Lopatulika likuti, "Cipindulo cace nciani, abale anga, munthu akanena, ndiri naco cikhulupiriro, koma alibe nchito?" (Yakobo 2:14.) Yesu adati, "Ngati mukonda Ine sungani malamulo anga." (Yohane 14:15).

Ndi capafupi kunena, "Ndili mkristu." Koma tionetsa anthu ena kuti tilidi akristu m'makhalidwe athu. Mau athu a pamtima a mcipangano cakale atiudza kuti ngati timvera Mulungu tidzakhala ace.

M'cipangano catsopano tiudzidwa kuti pamene Yesu adakhetsa mwazi wace kamba ka ife, anatigula kukhala ace. "Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu."



| | |
|---|---|
| Lacinai | Aroma 6:23 |
| Lacisanu | Miyambo 10:18 |
| Loweluka | Mateyu 12:34 |
| Lasabata | Yohane 14:6 |

Kunong'ona zimene zionongа dzina la munthu wina ndi koipa. Kunena-nena za anthu ena kungaononge maina ao. Kunamizira ena kungabweletse mabvuto. Kumabweletsa maganizo oipa. Kunama kupangitsa kuti anthu ena asamukhulupirire munthu wonamayo. Ndi nkhani yoopsya kwambiri.

Yesu adati, "...pakuti m'kamwa mungolankhula mwa kusefuka kwace kwa mtima." (Mateyu 12:34) Kulankhula zonama kucokela ku mtima wonama. Ucimo onse uyamba ndi mtima umene suli pa ubale wabwino ndi Mulungu. Ngati mitima yathu ndi yodzuzidwa ndi ubwino ndiponso cikondi ca Mulungu, idzazuzidwanso ndi cikondi ndiponso ubwino kwa anthu ena.

Ngati tili ndi cikondi coona m'mitima yathu pa anthu ena, sitingakhale mboni zonama kwa anthu ena. Tiyenela kuyang'ana mitima yathu nthawi zambili. Tiyenela kulankhula zoona cabe nthawi zonse.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Tiyeni tiyang'anisise miyoyo yathu lero. Tiyeni tidzifunse ngati sitimvera lamulo la Mulungu. "Usam'namizire M'nzako."

Mkristu ayenela kukhala monga Kristu. Yesu adati, "Ine ndine ... coondadi" (Yohane 14:6). Monga akristu tiyenela kulankhula zoona cifukwa Kristu akhala mwa ife. Ngati timulola kuti alamulire miyoyo yathu, tidzalankhula zoona cifukwa iye ndi coonadi.

PEMPHERO: Pempherani kuti tione kunama ndi ucimo. Pempherani kuti tidzalole Kristu kulamulira miyoyo yathu ndi kuti tidzadzidwe ndi ubwino ndiponso coonadi.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinito 3:9

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:16 |
| Laciwiri | Miyambo 6:16-19 |
| Lacitatu | Yohane 8:44 |



1 Akorinto 6:19, 20.

Tili a Mulungu. Anatigula ndi mwazi wa mwana wace. Tionetsa cikondi cathu kwa iye pokhala moyo wolungama ndi pomvera malamulo ace. Iyi ndiyo njira imene timulemekedzera m'mathupi athu.

GAWO LACITATU: Tiyeni tiwelenge m'Buku Lopatulika kuti tione zimene anthu adacita Mose atapatsidwa malamulo khumi. (Welengani Eksodo 24:3-8.)

Mose anawaudza anthu zimene Mulungu adanena. Anthu adafuula, "Zonse zimene Ambuye anena tidzacita ndipo tidzamvera."

Ndi cofunika kwambiri m'mene tiyankhira ku mau a Mulungu. Ndi cofunika kwambili m'mene tiyankhira ku zimene Mulungu atituma kuti tidzicite. Pamene Buku Lopatulika lilankhula kwa ife, kodi tiyankhula bwanji? Kodi timati, "Zonse zimene Ambuye anena ndizacita?" Iyi ndiye njira yabwino yoyankhira Mulungu.

Pamene timvera mau a Mulungu adzakhala nyali ndi mphamvu m'miyoyo yathu. Ngati timukondadi Mulungu, tidzakonda malamulo ace. Tidzamvera mwamsanga ndi kucita zonse zimene anena.

GAWO LACINAI: Yesu adati, "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula cilamulo kapena aneneri: Sindinadze kupasula, koma kukwaniritsa." (Mateyu 5:17). Malamulo khumi akali athu lero. Ationetsa zimene Mulungu ayembekedzera kwa anthu ace. Ndi oyambilira pophunzitsa za Mulungu kuti anthu adzikhala moyo wau Mulungu.

Ngati mwana wa m'ng'ono abwela pafupi ndi moto, timati, "iai, iai." Atakulako timuudza kuti moto udzamuyocha.

M'malamulo oyamba a Mulungu, asanu ndi atatu akuti, "Iai, iai." Atiudza kuti tisa-

cite zinthu zina. Pamene tikula m'miyoyo yathu ya cikristu, timvetsa bwino. Pamenepo tidzamvesa bwino cifukwa cace tiletsedwa kucita zinthu zina. Ngati timvetsa kwambiri za Mulungu tidzapitiriranso kumukonda. Tidzafuna kumvera cifukwa timukonda kwambiri.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Kwa milungu khumi ikubwerayi tidzakhala tili kuphunzira malamulo khumi. Mulungu ayembekedzera kuti tidzimulemekedza. Ayembekedzera kuti tidzimvera malamulo ace. Kodi tili okonzeka kucita cimene anena?

Tili okonzeka kunena tsopano kwa Mulungu, "Zonse zimene mudzanena ndidzacita?" Tiyeni tiganidzire kwambiri za zimenezi pamene tikumbukira mau a Yesu amene taamva kale lero, "Ngati mukonda ine mudzasunga malamulo anga." (Yohane 14:15).

PEMPHERO: Tiyeni tipemphere kuti ali yense wa ife adzazipeleka kwa Ambuye. Tiyeni tipemphere kuti timukonde kwambiri kuti titsunge malamulo ace.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9

ZOWELENGA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 19:5 |
| Laciwiri | Aefeso 2:8-9 |
| Lacitatu | Yakobo 2:14 |
| Lacinai | 1 Akorinto 6:19-20 |
| Lacisanu | Eksodo 24:3-8 |
| Loweluka | Mateu 5:17 |
| Lasabata | Yohane 14:15 |



GAWO LACITATU: Kunama ku nayamba m'munda wa Edene. Satana m'maonekedwe a njoka anamunamiza Adamu ndi Hava. Hava adakhulupilira bozalo. Sanamvere Mulungu ndipo cimo loyamba lidalowa mdziko lapansi.

Satana ndiye ciyambi ca maboza onse. Akuitanidwa tate wa maboza. Mu Yohane 8:44 Yesu adati, "... Inu muli ocokera mwa atate anu mdierekezi, ndipo zolakalaka zace za atate wanu mufuna kucita. Iyeyu anali wombada kuyambira paciyambi, ndipo sanaime m'coonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wace; pakuti ali wabodza, ndi atate wace wa bodza."

Anthu ena amanama pofuna kulewa zotsatira zimene zingabwele ngati anena zoona. Ena amanama cifukwa codzikonda. Ali odzikonda kwambiri kunena zoona. Ena amanena cifukwa ndi mkhalidwe wawo wonama. Amaonetsa mkhalidwe wawo. Mkhalidwe wonama ucokera kwa satana.

Ena amanama kuti akhale osiyana ndi anzao, kuti anthu adzimvera kwa iwo, kapena kuti anthu awacitire cifundo. Ena amanama pofuna kudziika pabwino ndi kuika anzao poipa. Ena nthawi zonse amanama kuti anaiwala kunena zoona. Boza limodzi lipitisa kulina kufikira kuti anthu sankatha kudziwa bwino ngati munthuyo akamba zoona kapena ai. Kwa iwo zoona zili pamodzi ndi zonama.

Zifukwa zonse zonamila zicokera ku cifukwa cimodzi.. Ucimo. Tinganame pofuna kuti anthu atsatione kulakwa kwathu, koma "Mphotho ya ucimo ndi imfa." (Aroma 6:23). Tsiku lina tidzakomana ndi ciweruzo ca Mulungu.

GAWO LACINAI: Njira imodzi yonamila ndi kucitira umboni wonama ndi kunena zinthu zimene si zili zoona koma onenayo afuna kuti aononge dzina labwino la munthu winayo. Mau a Mulungu akuti, "Wobisa udani ali ndi milomo yonama; wonena ugogodi ndiye citsiru." (Miyambo 10:18) Awa ndi mau akuru, koma ndi mau a Mulungu.

ndi adani ace zidanena zonama. Mulungu mu mau ace akuti kuda "Mboni yonama yonong'ona maboza." (Miyambo 6:19).

Nthawi zina munthu angakhale cete komabe angakhale mboni yonama. Tingamve munthu wina alinkupatsa mlandu munthu wina. Pamene timvera, tingadziwe kuti mlanduwu ndi wonama. Koma ngati tifuna kuti munthuyo abvutike, tingakhale cete. Ngati ticita zinthu zotere ticita umboni wonama. Tingapangitse kuti munthu wina abvutika pamene tinkayenela kulankhula zinthu zoona. Ici ndi colakwa.

Tingacitirenso umboni wonama pamene tinena cabe gao la zoona. Tingaonetse zonama zimene zinacitika pamene tilankhula cabe gawo la zimene zidacitika. Anthu ena atembenuza zoona pang'ono cabe kuti zikhale monga ndi zosiyana kwambiri.

Njira zonsezi zokhalira mboni zonama ndi zolakwa. Ndi ucimo kwa Mulungu.

GAWO LACIWIRI: Tingaone makolo amene aphunzitsa ana ao kuti azinama. Sanena "Ndi cabwino kunama." Aphunzitsa kunama ndi cisanzo, pa zimene iwo acita. Nthawi zambiri ana amapita ku sukulu ndi kukanena nkhani yonama. Angachule zaka zonama. Kapena kupeleka cifukwa conama cimene sanabwelele ku sukulu.

Ana adziwa ngati makolo ao anena zoona. Nthawi zina makolo angakhale ndi mwana kuti adzimunamira. Ana sangaphunzire kukhala okhulupirika ndi kulankhula zoona ngati makolo acita zinthu zotere.

Ana ang'ono nthawi zina amanena maboza. Nthawi zambiri amanena cinenenene. Kapena amanama pafuna kubisa colakwa cimene acita. Anganame pofuna kuti makolo asadziwe cinthu cina cimene safuna kuti acidziwe. Ana ngati anama ayenera kuudzidwa kunama ndi kulakwa. Ayenela kuphunzitsidwa kuti adzilankhula zoona cabe nthawi zonse.



PROGRAMU 2

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: OSATI MILUNGU INA.

MAU A PAMTIMA:
*"Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha."*

*Eksodo 20:3*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Taphunzirani lamulo loyamba monga mau athu a pamtima lero. Ndi lakuti "Usakhale nayo milungu ina koma ine ndekha." Eksodo 20:3. Anthu a ku Israyeli anali akapolo ku Aigupto. Anaona Aigupto ali kupembedza milingu yosiyanasiyana. Tsopano Mulungu anawaudza kuti Iye ndiye anali Mulungu oona basi. Anaudzidwa kuti asapembedze milungu ina.

Lero tidzaphunzira cimene lamulori litanthaudza kwa ife monga akristu.

GAWO LOYAMBA: Buku Lopatulika litudza ife kuti Mulungu akuti, "Ine ndiri Yehova, ndipo palibe winanso; popanda ine palibe Mulungu..." (Yesaya 45:5). Pali Mulungu m'modzi cabe woona. Palibe Mulungu wa anthu a ku Japani kapena Mulungu wa ku Afrika kapenanso Mulungu wa azungu.

Pali Mulungu m'modzi cabe. Ndi wamkulu kwambiri. Ndi wodalitsidwa ndipo wopanda cimo. Ali wa mphamvu zonse. Ndi mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye. Ndi Iye yekha amene afuna cikondi cathu conse.

M'neneri Eliya analankhula kwanthu amene anali kupembedza mulungu onama ochedwa Baala. Anawaudza kuti asankhe kutumikira Mulungu kapena Baala. Adati, "...ngati Yehova ndiye Mulungu, mtsateni Iye; ngati Baala, mumtsate iyeyo." (1 Mafumu 18:21).

Yesu adati munthu sangakhale wanchito kwa anthu awili. Mateyu 6:24. atiudza ife mauwa a Yesu, "Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri; pakuti pena adzamuda m'modziyo, ndi kukonda winayo; pena adzakangamira kwa m'modzi, nadzanyoza wina..."

Ngati tisankha kutumikira Mulungu, tiyenela kumuika poyamba. Tiyenela kumutumikira yekha basi. Sitingathe kutumikira Mulungu ndi dziko lapansi pa nthawi imodzi.

GAWO LACIWIRI: Ciri conse cimene ndi coyamba pa miyoyo yathu ndico Mulungu wathu. Akristu amene saika Mulungu kukhala oyamba pa moyo wao samvera lamulo loyamba. Pali zinthu zambiri zimene anthu aika zoyamba pa miyoyo yao. Anthu ena amakonda ndalama koposa kanthu kena kali konse. Ena amakonda ndalama koposa kuti akhoza ndi kunama kapena kuba kuti adzipedze. Akristu ambiri amakana kupeleka cikhumi cao kwa Mulungu. Amakonda ndalama koposa m'mene amakondera Mulungu.

Anthu ena amaika maphunziro kukhala oyamba pa miyoyo yao. Anthu ena amaika nyumba zao kapena mabanja ao kapenanso zilakolako zao kukhala zoyamba. Anthu ena amaika zinthu kukhala zoyamba, monga zobvala zabwino kapena galimoto. Ambirinso amaziika eni ace poyamba, kufuna kudzikondweretsa okha basi osaganizilanso za anthu ena.

Ngati tikonda zinthu koposa m'mene tikondera Mulungu, sitimvera lamulo la Mulungu, "Usakhale nayo milungu ina koma ine ndekha."

GAWO LACITATU: Ana a Israyeli nthawi zina anali kumuiwala Mulungu. Anayamba kucita ucimo ndi kutumikira milungu ina. Nthawi zonse zimene anali kucita ucimo Mulungu anali kuwalanga kamba ka ucimo wao. Nthawi zonse zimene anali kucita macimo anali m'mabvuto oopsya. Potsiridzira, anatengedweranso mu ukaporo ndi mapfuko amphamvu.





COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KULANKHULA BWINO.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:
*"Usam'namizire m'nzako."*
*Eksodo 20:16*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Lamulo limene tidzaphunzira lero litiudza kuti tisacitire umboni wonama. Ici citanthauza kuti tisaname. Tinganene kuti lamuloli litanthauza: Uzakamba zoona nthawi zonse, pali ponse.

Lamuloli ndi lofunika kuti tikhale okondwa ndiponso kuti tidzicitira bwino umboni wa cikristu. Mau a Mulungu ali ndi zambiri zonena zokhuza malilime athu. Miyambo 6:16-19 atiudza kuti, "Ziripo zinthu zisanu ndi cimodzi Mulungu azida; ngakhale zisanu ndi ziwiri zim'nyansa. Maso akunyada, lilime lonama, ndi manja akupha anthu osacimwa; mtima woganizira ziwembu zoipa, mapazi akuthamangira mphulupulu m'mangu m'mangu; mboni yanama yonong'ona mabodza, ndi wopikisanitsa abale." (Miyambo 6:16-19.)

Mulungu akuda kunama, mnjira ili yonse.

GAWO LOYAMBA: Kupeleka umboni wonama kungacitike mu khoti pa nthawi ya mlandu. Anthu ena azacita cimeneci pofuna kuthandidza m'nzao kapena mbale wao. Uku ndi kulakwa kwambiri ndipo ndi ucimo kwa Mulungu. Ngati tiitanidwa kuti ticitire umboni mu khoti, tiyenela kulankhula zimene tidzindikira kuti ndi zoona.

Anthu ena ayesa kupatsa munthu ndalama kuti akanene boza mukhoti. Pa mulandu wa Yesu mboni zonama zimene zidapatsidwa ndalama

Tiyeneranso kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Buku Lopatulika likuti tibela Mulungu ngati sitipeleka cikhumi cathu. (Welengani Malaki 3:8-10.) Akristu ambiri m'machalichi athu ndi osakhulupirika popeleka cikhumi cao.

Tiyeni tiganizire kwambiri ngati tili okhulupirika m'njira zonse.

PEMPHERO: Pempherani kuti Mulungu atithandize kusuka mitima yathu ndi miyoyo yathu ku kusakhulupirika kuli konse. Pempherani kuti akristu adzaone kufunika kopatsa Mulungu cikhumi cao ndi kuthandiza mipingo yao.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9.

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:15 |
| Laciwiri | Mateyu 4:4 |
| Lacitatu | Mateyu 6:33 |
| Lacinai | Luka 19:8 |
| Lacisanu | Aefeso 4:28 |
| Loweluka | Yohane 14:15 |
| Lasabata | Malaki 3:8-10 |



Buku Lopatulika likuti, "Musanyengedwe, Mulungu sanyozeka, pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzacituta. (Agalatiya 6:7). Tikhodza kunyenga ena, koma Mulungu adziwa zonse. Mulungu adziwa ngati timukonda Iye kopambana zinthu zina zonse. Adziwa cimene cili coyamba m'moyo yathu ndi m'mitima yathu. Adziwa zonse zimene tiganidzila.

Ife eni ace tisankhula njira imene tidzapitamo. Cimene Mulungu anena nthawi zonse ndi cabwino. Kupita njira yathu kudzatitsogolera ku kutsakondwa ndipo pothera pace ku cionongeko. "Pakuti mphotho ya ucimo ndi imfa." (Aroma 6:23). Ngati Mulungu sindioyamba m'miyoyo yathu, tidzabvutika ndi kutsamvera malamulo ace.

GAWO LACINAI: Buku Lopatulika litiudza kuti Mulungu adati kwa anthu, "Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye m'modzi; ndipo mudzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba." (Mateu 22:37-38).

Akristu alamulidwa kukonda Mulungu ndi mitima yao yonse. Sitingatsunge malamulo ena ngati sititha kukonda Mulungu koposa zinthu zina zonse. Ndi cofunika kuti sitipha kapena kuba kapena kusilila kapena kucita cigololo. Komabe, tili ocimwa. Sitingathe kukhala ndi moyo wolungama kopanda thandizo la Mulungu.

Tingakhale ndi mphamvu ya Mzimu Woyera kuti igonjetse mayesero ndi ucimo ngati tilola kuti Mulungu akhale mwa ife. Tingapambane pa miyoyo yathu pokhapo ngati mzimu woyera ulamulira m'miyoyo yathu.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Kodi tikuika milungu ina patsogolo pa Mulungu? Kodi ndi ciyani cimene tikonda koposa? Kodi Mulungu ndi oyambilira m'mitima yathu? Kodi mzimu woyela ulamulira m'miyoyo yathu?

Tiyeni tiganidzire kwambiri mafunsowa. Ngati Mulungu sindioyamba m'mitima yathu, lero tingamuudze kuti akhale oyamba ndi kuti akhale Mbuye wa miyoyo yathu yonse.

PEMPHERO: Pempherani kuti tisakhale ndi milungu ina koma m'modzi woona. Pemphelerani mphamvu zosiira zinthu zonse zimene zitilepheletsa kuti Mulungu akhale oyamba m'miyoyo yathu.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA INO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:3 |
| Laciwiri | Yesaya 45:5 |
| Lacitatu | 1 Mafumu 18:21 |
| Lacinai | Mateyu 6:24 |
| Lacisanu | Agalatiya 6:7 |
| Loweluka | Deutoronomo 6:4-5 |
| Lasabata | Mateyu 22:37-38 |



Ngati tikhukupirira Mulungu ndi kumuika poyamba, Mulungu alonjeza kutipatsa zonse zosowa zathu monga mwa cikondi cace ndi cifuniro cace. Tiyenela kutsatira njira yace, Tiyenera kumvera lamulo lace. Adzatipatsa zonse zimene zitisowa.

GAWO LACINAI: Pali njira zambiri zotsamverera lamuloli, "Usabe." Wa malonda angabe kwa anthu ogula pamene sawapatsa yonse cenji. Nthawi zina anganene kuti awagulitsa nyama ya makilo awiri koma awapatsa nyama kilo limodzi ndi theka. Mzimai amene agulitsa nsalu angaike yoipa pansi kuti isaoneke. Uku ndi kutsakhulupirika ndipo ndi ucimo.

Kunama ku sukulu kapena pa masewela ndi gao lina la kuba. Wina angabe ngati salipira bwino anchito ace. Kukhulupirika kuli konse ndi koipa.

M'Buku Lopatulika tiuzidwa za Zakeyo. Anali kawalala cifukwa anali kutenga msonkho wambiri koposa m'mene anali kuyenera kutengera ndipo anali kusunga ndalama za pamwambazo. Sanaone kuti uku kunali kunama. Inali njira yopedzera ndalama. Tsiku lina Zakeyo adakomana ndi Yesu. Adamukhulupirira. Pamenepo adakhala munthu watsopano. Adati, "...Taonani, Ambuye, gawo limodzi la zanga zonse zogawika pakati ndipatsa osauka; ndipo ngati ndalama kanthu kwa munthu monyenga, ndi mbwezera kanai." (Luka 19:8)

Ngati tisatiladi Yesu, sitingapitilize kukhala osakhulupirika, Mtumwi Paulo adati, "Wakubayo asabenso..." (Aefeso 4:28). Ngati taba tiyenera kubwedza. Tiyenera kupanga zinthu kukhala zabwino m'manso a Mulungu ndi munthu. Pambuyo pace tisakhalenso osamvela.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Yesu adati, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." (Yohane 14:15). Kukhulupirika ndiye njira ya cikondwerero coona. Tiyenera kukhala okhulupirika kwa ife eni ace ndi ku anthu ena.

mvera mau ace.

GAWO LACITATU: Tidziwa kuti Mulungu safuna mwana ali yense kapena munthu ali yense kuti adzibvutika cifukwa ca njala kapena zosowa zina. Koma, afuna kuti tidzigwiritsa nchito njira zabwino popedza zinthu zimene tifuna pa miyoyo yathu.

M'mateyu, mutu 5 ndi 6, tapasidwa mau amene Yesu adanena kwa anthu ambili amene anali kumutsatira. Adati kuti Mulungu adziwa zonse zosowa zathu zathupi. Tiyeni timvere ku mau a Yesu:

> "...Cifukwa cace ndinena kwa inu, musadere nkhawa moyo wanu, cimene mudzadya ndi cimene mudzamwa; kapena thupi lanu, cimene mudzabvala. Kodi moyo suli woposa cakudya, ndi thupi loposa cobvala? Yang'anirani mbalame za kumwamba, kuti sizimafesa ai, kapena sizimatema ai, kapena sizimatutira m'nkhokwe; ndipo Atate wanu wa kumwamba adzidyesa. Nanga inu mulibe kusiyana nazo kuziposa kodi? Ndipo ndani wa inu ndi kudera nkhawa angathe kuonjezera pa msinkhu wace mkono umodzi? Ndipo muderanji nkhawa ndi cobvala? Tapenyetsani maluwa a kuthengo, makulidwe ao; sagwiritsa nchito, kapena sapota; Koma ndinena kwa inu, kuti angakhale Solomo mu ulemerero wace wonse sanabvale monga limodzi la amenewa. Koma ngati Mulungu abveka cotero maudzu a kuthengo, akhala lero, ndi mawa oponyedwa pamoto, nanga si inu kopambana ndithu, inu akukhulupirira pang'ono? Cifukwa cace musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya ciani? Kapena, Tidzamwa ciani? Kapena, Tidzabvala ciani? Pakuti anthu akunja azifunitsa zonse zimenezo; pakuti Atate wanu wa kumwamba adziwa kuti musowa zonse zimenezo. Koma muthange mwafuna ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu." (Mateyu 6:25-33)



PROGRAMU 3.

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULC KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KUPEMBEDZA KOONA KWA MULUNGU WOONA.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"Usadzipangire iwe wekha fano losema."*

*Eksodo 20:4.*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Lero tidzaphunzira lamulo laciwiri. Lamulo loyamba linatiphunzitsa kuti Mulungu ayenela kukhala oyamba m'miyoyo yathu. Sitiyenela kupembedza timilungu tonama.

Ndi cofunikanso m'mene tipembedzera Mulungu m'modzi woonayo. Lamulo laciwili litiudza ife kuti tisagwadire mafano a mitundu uli onse.

Tiyeni tiwelenge bwino lamulo limeneli. (Welengani Eksodo 20:4-6).

GAWO LOYAMBA: Kodi fano ndi ciyani? Fano ndi cinthu cili conse cimene munthu akhulupirira kuti cingamuthandidze kapena kuti angapedzeko cipulumutso. Mafano ena akupangidwa ndi mitengo. Ena akupangidwa ndi zisulo kapenanso miyala.

Mu Yesaya, mutu 44, tiudziwa za munthu amene atenga mtengo mthengo. Nkhuni zina amapangira moto kuti asamve mphepo. Nkhuni zina amaphikira cakudya. Nkhuni zinanso amapangako fano. Amagwadira fanolo.

Anapanga fanolo ndi manja ace. Koma akhulipirira kuti lidza muthandidza ndi kuyankha mapemphero ace. Akuti kwafano losemalo "Ndipulumutse ine, cifukwa kuti ndinu Mulungu wanga." (Yesaya 44:17) Kodi mtengowo ukamuthandidzadi munthuyo? Siu... kamuthandidza, cifukwa unalibe muthengo basi.

Tidziwa anthu lero amene akhulupirira kuti zinthu zotere zingawathandidze. Ena akhulupirira m'mankwala otetedzela mwana. Ena amagula mankwalawo kuti adzipambana kwambiri m'maphunziro ao kapena kuwathandidza m'njira zina. Satana agwiritsa nchito zinthu zotere pofuna kucotsa cikhulupiriro cathu pa Mulungu.

Mulungu sakondwera ndi zinthu zotere. Atiudza ife mosakaika, "Usadzipangire iwe wekha fano losema." (Eksodo 20:4)

GAWO LACIWIRI: Ena amati mafano awathandidza kuganidzira za Mulungu. Buku Lopatulika likuti "Mulungu ndiye Mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira m'mzimu ndi m'coonadi. (Yohane 4:24). Sitiyenela kukhala ndi fano kuti litikumbutse Mulungu. Sitifuna fano kuti tipembedze Mulungu.

Buku Lopatulika litiudza kuti ngati tili akristu Mulungu akhala mwa ife. "Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu?" (1 Akorinto 6:19). Mulungu nthawi zonse ali ndi ife cifukwa akhala mwa ife. Nanga cifukwa ninji coti tikhalire ndi fano kuti tikumbukire Mulungu? Ici sicikondweretsa Mulungu.

Mverani kumauwa amene acokera mu 1 Yohane 5, ndime 20 ndi 21: "Ndipo tidziwa kuti mwana wa Mulungu wafika, natipatsa ife cidziwitso kuti tizindikire woonayo, ndipo tiri mwa woonayo, mwa mwana wace Yesu Kristu. Iye ndiye Mulungu woona ndi moyo wosatha. Tiana, dzisungire ni nokha kupewa mafano."

Ili ndilo lamulo la Mulungu kwa ife. Mulungu woona ndi Mulungu omvera. Tili ndi moyo wosatha kudzela mwa Yesu Kristu, mwana wa Mulungu. Sitiyenela kupanga kapena kugula fano liri lonse. Sitiyenela kukhala ndi mafano m'nyumba zathu kapena m'machalichi athu. Sitiyenela kugwiritsa nchito mafano popembeza Mulungu woona.



adzikhala.

Akuba ndi umbombo ndipo afuna kuti zinthu zonse zidzikhala zao. Sacitapo ubwino kwa munthu ali yense. Kuba nthawi zonse kupitilidza ku kunama ndi ku kumenyana - menyana. Kawalala nthawi zonse akhala mwa mantha, cifukwa aopa kuti tsiku lina adzapedzedwa. Kuthera kwace kwa kawalala ndi kuti agwiridwa ndipo atumidwa ku ndende.

GAWO LACIWIRI: Kodi ndi cifukwa ninji anthu amaba? Nthawi zina munthu angabe kamba kanjala nchito sadziwa munthu aliyense amene angamuthandidze. Nthawi zina munthu amaba cifukwa ali ndi abwenzi oipa amene amunyenga kuti adzilakwira pamozi. Anthu ambiri aumilidzidwa kuti athandidze kuba cifukwa satha kukana.

Anthu ena amaba kamba kosilila. Safuna kuona anthu ena alinkupita patsogolo. Safuna kuona anthu ena amene ali ndi zinthu zimene iwo afuna koma alibe.

Ena amaba cifukwa ca ulesi. Ndicapafupi kwambiri. Munthu akuti, "Cifukwa ninji ndigwira nchito? Ndingapedze zimene ndifuna. Ndingakondwere. Ndingakhale ndi zobvala zabwino ndiponso mowa. Ndingakhale ndi abwenzi ndiponso ndalama."

Ena adziganidzira eni ace, Ndili ndi zinthu zocepa kwambiri koma apa pali zambiri. Ndi cabwino ngati ndingatengepo pang'ono cabe.

Ndi satana amene audza munthu zinthu zotere. Kuba ndi kucimwira Mulungu. Satana adabwera kumuyesa Yesu kuti acimwe pamene Yesu adali mcipululu ndipo anali ndi njala kwambiri. Yesu anakana angakhale kumvera cabe. Anati kwa satana: "Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu." (Mateyu 4:4).

Buku Lopatulika linena poyera "Usabe." Mu maso a Mulungu palibe cifukwa cabwino cosa-

PROGRAMU 9

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: "USABE."

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:
*"Usabe."*

*Eksodo 20:15*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Lamulo tidzaphunzira lero likhudza kukhulupirika. Litiphunzitsa kuti tiyenela kukhala okhulupirika kwa ife eni ace ndi kwa anzathu. "Usabe," atero Mulungu kwa ife.

Kuba kutanthaudza kuti cinthu ca mwini. Buku Lopatulika likuti kuba ndi ucimo.

Lero tidzaphunzira cimene lamuloli litanthaudza kwa ife.

GAWO LOYAMBA: Kodi wakuba ndi ndani? Wa kuba kapena kawalala akuti, "Ndi citsiru cabe amene ankatsewedza kuti apedze ndalama zofunika pa moyo wace. Ngati uli ocenjera ungapedze zimene ufuna osagwira nchito."

Kuba kungacitike polowa m'nyumba ya mwini kapena kutenga zinthu mu thumba la thilauza la mwini kapena kulanda cikwama ca mwini. Wakuba angakhale woba galimoto kapena njinga. Angatenge mfuti kuti adziumilidza anthu kuti anthu kuti adzimupatsa zimene afuna. Angamenye anthu, natenga ndalama zao ndi kuwatsiya kuti adzibvutika.

Nthawi zambiri kawalala aganidzila kuti ndi ocenjela kwambiri. Aganidzila kuti angapedze ndarama zambiri posazigwirira nchito. Amapangitsa anthu ena kukhala aumphawi pamene iye alemela. Amasamila pa anthu ena kuti



GAWO LACITATU: Lamulo laciwiri litiphunzitsa cinthu cimodzi monga comwe tiphunzitsidwa ndi lamulo loyamba. Ici ndico cakuti Mulungu ayenela kukhala m'moyo wa mkristu.

Mulungu adati, "Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje..." (Eksodo 20:5). Ici citanthaudza kuti Mulungu safunanso aliyense kuti adzigawana naye malo m'mitima yathu ndi m'cikondi cathu. Munthu amene ali ndi akazi awiri ayenera kugawa cikondi cace pakati pa akaziwo. Sangathe kukonda m'modzi ndi mtima wace wonse. Akhodza kukonda mkazi m'modzi ndi gao la mtima wace basi. Ici cibweletsa nsanje ndiponso mabvuto kwa mwamuna ndi akazi ace.

Mulungu akuti sitingathe kumukonda mujira yotereyi. Sadzalola zotere, pakuti Iye ndi Yehova wa nsanje. Akuti tiyenela kumukonda ndi mtima wathu wonse. Amene apembedza milungu ina kapena mafano adzalangidwa.

Lamuloli litionetsa m'mene Mulungu atikondera. Ngati mkazi akonda kwambiri mwamuna wace, safuna kuti mwamunayo akhalenso ndi akazi enanso. Mulungu atikonda munjira yotere. Sadzagawana ndi aliyense cikondi cathu ndiponso kumvera kwathu.

Ngati timukondadi Mulungu, sitidzafunanso kukonda zinthu zina kopambana. Tidzakhala okondwa kuika Mulungu kukhala oyamba m'miyoyo yathu. Tidzadziwa kuti ndi njira yokhayi yacikondwerero coonadi ndi mtendere.

GAWO LACINAI: Ndi satana amene atiyesa kuti tidzikhulupirira m'mankhwala kapena mafano kapena zinthu zinanso. Satana ali ndi mphamvu kwambirili. Buku Lopatulika litiudza ife kuti ndi mlungu wa dziko lino. Angatipangitse kuti tiganizire m'mitima yathu, "Ndidzakhulupirira Mulungu. Koma ndi kwabwino kuika mankhwalawa pa mwana wanga. Angacite coipa cotani?

Kapena satana anganene kwa ife, "Khulupirira mwa Mulungu. Koma pitirira ndi kupembedza mizimu ya makolo ako. Angakhale osakondwa." "Nthawi zina satana angatipangitse kuti tiganizire," Pemphera kwa Mulungu. Koma ng'anga ingakuthandidze ndithu. Bwanji sitipitako?"

Maganizo onse oterewa ndi maboza a satana. Amayetsa kuti ife tikhulupirire mzinthu zina pamodzi ndi Mulungu.

Bwanji ngati munayetsa, koma simungathe kusiya zinthu zoterezi? Pempherani. Funsani anthu ena kuti apemphere nanu ndi kumupempherani. Mulungu ali ndi mphamvu zopotsa za satana. Atiudza ife kuti timukonde yekha basi ndi kumpempherani. Mulungu ali ndi mphamvu zopotsa za satana. Atiudza ife kuti timukonde yekha basi ndi kumpemphera yekhayo. Atiudza ife kuti tisiye mafano onse. Tingagonjetse satana ndi mphamvu za Mulungu basi.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Mulungu afuna cikondi cathu conse ndi kumvera kwathu konse. Kukhulupirira mu zinthu zina ziri zonse ndi kulakwa. Ciri conse cimene tiika m'malo a Mulungu ndi kulakwa. Mulungu akuti, "...iwo alibe nzeru, amene anyamula mtengo wa fano lao cosema, ndi kupmphera mlungu wosakhoza kupulumutsa. Nenani inu, turusani mlandu wanu; inde, acite uphungu pamodzi; ndani waonetsa ici ciyambire nthawi yakale? Ndani wanena ici kale? Kodi sindine Yehova? Ndipo palibenso Mulungu wina popanda ine. Mulungu wolungama, ndi mpulumutsi; palibenso wina popanda Ine. Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe, inu malekezero onse adziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibe wina." (Yesaya 45:20-22.)

PEMPHERO: Pempherani kuti tipemphere Mulungu m'modzi woona. Pempherani kuti timukonde ndi mtima wathu wonse.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9



Tisacimwe pokhala wosalungama m'makhalidwe athu kapena m'maganizo athu.

Tiyeneranso kuphunzitsa ana athu kuti cikwati ndi coyeletsedwa ndipo ndi cosadetsedwa. Tiyenera kuwaphunzitsa kuti cigololo ndi ucimo kwa Mulungu.

PEMPHERO: Pempherani kuti aliyense amene anacimwa pocita cigololo abvomeleze macimo ao ndipo akhululukiridwe. Pempherani kuti tonse tikhale miyoyo yoyela.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9.

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:14 |
| Laciwiri | Mateyu 19:4-6 |
| Lacitatu | Miyambo 6:32 |
| Lacinai | Mateyu 19:9 |
| Lacisanu | 1 Akorinto 6:9-11 |
| Loweluka | Mateyu 5:27-32 |
| Lasabata | Agalatiya 5:16 |

nela kukhala miyoyo yoyela.

GAWO LACINAI: Tsiku lina mzimai amene adagwiridwa alinkucita cigololo adabweletsedwa kwa Yesu. Atsogoleri a cipembezo amene anali kudziyetsa kuti anali abwino anali kuganidza kuti Yesu ankadzampatsa mlandu kamba ka cigololo. Linali lamulo lao kuti amene adali ndi mlandu wa cigololo aponyedwe miyala kufikira kufa. Koma Yesu anawayangana ndipo adati, "...Amene mwa inu ali wopanda cimo, ayambe kumponya mwala." (Yohane 8:7).

M'modzi-m'modzi anthu adapita. Pambuyo pace Yesu adati kwa mkazi "Pita; kuyambira tsopano usacimwenso." (Yohane 8:11). Pali cikhululukiriro kwa munthu amene acita cigololo. Buku Lopatulika litudza kuti "Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kuti sambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse." (1 Yohane 1:9)

Ndi cabwino kwambiri Kuti tisacite ucimowu. Pali njira yotitetedza ife kucita cigololo ndi kukhala miyoyo ysafunika. Buku Lopatulika likuti, "Muyende-yende ndi mzimu, ndipo musafitse cilakolako ca thupi." (Agalatiya 5:16). Ngati tsiku liri lonse tiyenda ndi mzimu, sitidzakhala ndi mlandu wocita zinthu zosalungama.

Tingaletsedwe ndi Mzimu Woyela. Poyamba, tiyenera kubvomereza macimo onse amene tidziwa m'miyoyo yathu, kudzipelekela kwa Yesu. Pambuyo pace tifunse Mzimu Woyela kuti ulamulire miyoyo yathu. Pambuyo pace tifunefune kutsatira cifuno cace tsiku lili lonse.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: "Usacite cigololo." Anthu ambiri lero akuswa lamuloli. Akristu ayenera kukhala ndi miyoyo yabwino, yosadetsedwa. Tisacimwe pokhala wosalungama m'makhalidwe athu kapena m'maganizo athu.

Tiyeneranso kuphunzitsa ana athu kuti cikwati ndi coyeletsedwa ndipo ndi cosadetsedwa.



ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:4 |
| Laciwiri | Yesaya 44:19 |
| Lacitatu | Yohane 4:24 |
| Lacinai | 1 Akorinto 6:19 |
| Lacisanu | 1 Yohane 5:20-21 |
| Loweluka | Edsodo 20:5 |
| Lasabata | Yesaya 45:20-22 |

PROGRAMU 4

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KULEMEKEDZA DZINA LA MULUNGU.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe."*

*Eksodo 20:7*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Maina ndi ofunika kwambiri. Makolo sachula cichulechule maina a ana ao. Maina anganene zambiri zokhudza munthuyo kapena banja lace. Dzina la munthu liimila mumalo a munthuyo.

Lero tidzaphunzira lamulo lacitatu. Litiudza kuti tidzilemekedza dzina la Mulungu. Lamuloli ndi mau athu a pamtima lero, Eksodo 20:7. Tiyeni tikambile pamodzi. (Nenani pamodzi Eksodo 20:7)

GAWO LOYAMBA: Ana a Israyeli anaona ndi kulemekedza dzina ndi umunthu wa Mulungu kwambiri. Ayuda ambiri sachula dzina la Mulungu. Ici ndi cifukwa cakuti anali kulilemekedza kwambiri dzina la Mulungu.

Mulungu ndi woyera. Mneneri Yesaya atiudza kuti anamuona Mulungu m'masomphenya. M'masomphenyamo adamva angelo alinkunena, "woyera, woyera, woyera, Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemerero wace." (Yesaya 6:3). Cifukwa Mulungu ndi woyera, Dzina lace ndi loyera.

Dzina la Mulungu liyenera kugwiritsidwa nchito motsamalira pamene tipemphera. Tiyenela kugwiritsa nchito dzina la Mulungu ngati timuthokodzadi. Lamulo lacitatu litiudza kuti ndi kulakwa kugwiritsa nchito dzina la Mulungu mosasamala. Ndi kulakwa kulankhula dzina la Mulungu



Munthu amene apitilidza ndi macimo ace sadzapulumuka, cifukwa Mulungu ndi woyera. Atiudza kuti ifenso tikhale oyera. Buku Lopatulika likuti, "...Nimukhale oyera; pakuti ine ndine Yehova Mulungu wanu." (Levitiko 20:7).

GAWO LACITATU: Yesu analankhulapo zokhudza lamuloli. Tiyeni tiwelenge zimene adanena zokhudza lamuloli. (Welengani Mateyu 5:27-32)

Yesu adati m'mene tiganizira m'mitima yathu za anthu ena zingatipangitse kulakwa. Cigololo ciyamba ndi zilakolako zoipa m'mitima yathu za anthu ena zingatipangitse kulakwa. Cigololo ciyamba ndi zilakolako zoipa m'maganizo ndi m'mtima. Yesu adati, "...yense wakuyang'ana mkazi kumkhumba, pamenepo watha kucita naye cigololo mumtima mwace." (Mateyu 5:28). Tiyenera kutsunga mitima yathu kukhala yoyela, ndi mathupi athunso.

Tiyenera kutsamara kuti siticita kanthu kena kamene kangabweletse cimo lina. Akazi angabvale munjira yopangitsa kuti amuna afune mathupi ao. Uku ndi kulakwa.

Lero pali mabuku ambiri, zinyimbo ndi zinthunzi-thunzi zimene zipangitsa amuna ndi akazi kuti adzazidwe ndi maganizo oipa. Munthu amene nthawi zonse aganizila cabe za cigololo acimwa m'mtima wace. Mawa tingacite zimene tiganidzira cabe lero.

Tiyenera kufunafuna abwenzi amene ndi abwino ndipo woyera. Tisapite ku malo a ucimo. Tisamvere ku nkhani zoipa. Tisakambe nkhani zonyansa.

Ngati tili akristu, mathupi athu ndi kacisi wa Mzimu Woyela. Tiyenela kuwatsunga kukhala abwino. Tisakhale ndi mlandu wocita cigololo. Tisakhale ndi mlandu wokhala ndi zilakolako zoipa, kapena kukamba zinthu zonyansa kapena kukhala ndi maganizo a umve. Tiye-

Cigololo ndi ucimo wa mwamuna amene agona ndi mkazi wa mwini pamene mwini mkazi palibe. Ndi ucimo wa mkazi amene adzankhala ndi cibwenzi pamene ali ndi mwamuna wace. Ndi ucimo wa mwamuna amene asiya mkazi wace ndi banja lace kutenga mkazi wina. Kapena ucimo wa mkazi amene asamala mwamuna wina. Ndi ucimo wa mkazi amene apeleka thupi lace kwa amuna kuti apedze ndalama.

GAWO LACIWIRI: Cifuniro ca Mulungu cinali cakuti mwamuna m'modzi akwatire mkazi m'modzi kufikira m'modzi wa iwowa atatengedwa ndi imfa. Ndi ucimo kwa mwamuna kukhala ndi akazi awili kapena atatu. Ici cimabweretsa mabvuto ambiri ndiponso nsanje m'nyumba. Cimapweteka ana pamodzi ndi makolo.

Ndi ucimo kwa mwamuna kusiya mkazi wace, kapena mkazi kusiya mwamuna wace. Yesu adati, "...Amene ali yense akacotsa mkazi wace, kosakhala cifukwa ca cigololo, nadzakwatira wina, acita cigololo." (Mateyu 19:9).

Mulungu atikonda. Afuna kuti tikhale ndi moyo wabwino koposa. Cigololo citipatsa kukhala ndi maganizo odzindikira kulakwa ndipo woopa. Cimapititsa ku kutsakondwa ndipo nthawi zina ku imfa.

M'nthawi ya m'cipangano cakale cigololo unali ucimo woopsya. Amene adali kucita cigololo anali kulangidwa ndi imfa. Lamulo la cipangano cakale cikuti, "Munthu akacita cigololo ndi mkazi wa mwini, popeza wacita cigololo ndi mkazi wa m'nansi wace, awaphe ndithu mwamuna ndi mkazi onse awiri." Levitiko 20:10.

Buku Lopatulika likuti wacigololo sadzapedza ufumu wa kumwamba. (Welengani 1 Akorinto 6:9-11.) Cigololo ndi ucimo waukhulu. Koma, Buku Lopatulika litiudza kuti ngati munthu wa cigololo kapena wocimwa aliyense alapa ndi kukhulupirira mwa Kristu, mwakhalidwe ace ocimwa ndi maganizo ocimwa adzacotsedwerathu.



polumbira kapena potukwana.

1 Dzina la Mulungu ndi loyera, monga momwe mwini wace alili woyera.

GAWO LACIWIRI: Tanthaudzo la lamuloli likhudza kupitilira zinthu zimene tachula. Likhudzanso m'mene tikhalira. Yesu adati, "Ndipo mundichuliranji Ine, Ambuye, Ambuye, ndi kusacita zimene ndizinena?" Luka 6:46. Kunena, "Ambuye, Ambuye" ndi cinthu coipa kwambiri ngati sitimutsatiradi Mulungu munjira zathu zonse.

Lero anthu ambiri adzatiuza, "O, Inde, Ndikhulupirira mwa Mulungu." Koma miyoyo yao iwontsa kuti samusamala Mulungu ngakhale pang'ono. Uku ndi kuchula dzina la Mulungu pacabe,

Anthu ena afuna kudziwika monga akristu. Koma safuna kupeleka malipiro ace kuti amutsatiredi Yesu. Monga akristu titenga dzina la Mulungu. Omutsatira oyamba Yesu anali kuchedwa aKristu cifukwa anali monga Kristu. Tichula dzina lace pacabe ngati sitikhala m'mene atiudzira kuti tikhalire.

Yohane atiudza, "Iye wakunena kuti, Ndimdziwa Iye, koma wosasunga malamulo ace, ali wabodza, ndipo mwa Iye mulibe coonadi; koma Iye amene akasunga mau ace, mwa iyeyu zedi cikondi ca Mulungu cathedwa. M'menemo tidzindikira kuti tiri mwa Iye; iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wace kuyenda monga anayenda Iyeyo." (1 Yohane 2:4-6).

Yesu adati, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." (Yohane 14:15).

GAWO LACITATU: Lero anthu ambiri ali otayika popanda Mulungu. Tiyenera kukhala okonzeka potsatira Yesu. Yesu adati, "Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenga mtanda wace, nanditsate ine." (Mateyu 16:24)

Kodi Yesu anali kutanthaudza ciani? Anali kutanthaudza kuti ngati tinena zoona kuti tidzamusata, tiyenela kufa kwa ife tokha. Tiyenera kupaya zilakolako zathu kuti ticite cokhaco cimene Iye afuna.

Ici cioneka monga cinthu colimba kucicita. Koma Yesu akuti, "Koma Iye amene ataya moyo wace cifukwa ca ine, adzaupeza. Pakuti munthu adzapindulanji, akalandira dziko lonse, nataya moyo wace? Kapena munthu adzaperekanji cosintha ndi moyo wace?" (Mateyu 16:25, 26).

Kodi mufuna kupedza moyo woonadi? Lesani zilakolako zanu, ndipo ikani Mulungu kukhala woyamba pa moyo wanu. Mudzapedza moyo waukulu. Mudzakhala muli kulemekenzanso dzina la Mulungu.

**GAWO LACINAI:** Kodi kunkacitika ciani ngati akristu onse anali kuyamika dzina la Mulungu m'njira imene tilankhulira ndi m'mene tikhalira? Kodi kunkacitika ciani ngati akristu onse anali kumutsatira Mulungu mu zinthu zonse?

Pankakhala cikondi cosaneneka pakati pa akristu. Mkwiyo, nsanje, kudana ndi kumenyana zinkatha. M'kristu ali yense ankafuna cimene ndi cabwino kwa anzake basi, osaganizira za mwini wace.

Pankakhala ndalama zambiri kupititsira patsogolo nchito ya Mulungu. Akristu ankapeleka ndalama zao ndi kugawana ndi anzao. Abusa ankathandidzidwa. Machalichi ankanamangidwa. Anthu a mishone ankatumidwa m'dziko lonse lapansi kuti akalalikire uthenga wabwino.

Amene anali akristu ankanaona kuti Mulungu ali woona. Ankanamuona m'miyoyo yathu. Ankanabwera kwa Iye ndi kupulumutsidwa. Kodi ici ndi colimba?

Buku Lopatulika litudza ife mu Macitidwe, mutu 2, zakubwera kwa Mzimu Woyera. Pamene akristu anadzazidwa ndi Mzimu Woyera, anali ndi mphamvu yaikulu yolalikira ndi kucitira umboni.



## PROGRAMU 8

**COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.**

**COPHUNZIRA LERO: KUFUNIKA KOKHALA WOSADETSEDWA.**

**NTHAWI YA PEMPHERO:**

**MAU A PAMTIMA:**
*"Usacite cigololo."*
*Eksodo 20:14*

**MTSOGOLERI WA PROGRAMU:** Lamulo limene tidzaphunzira lero litiudza, "Usacite cigololo." Cigololo cimacitika ngati mwamuna ndi mkazi akhala pamozi zosafunika zina zonse. Amuna, akazi ao ndi amene ali osakwatiwa ndi kukwatira angacite cigololo. Lero anthu ambiri atseka malamulo a Mulungu okhudza kukhala wosadetsedwa. Koma tidzaona kuti mau a Mulungu ndi omveka bwino pa miyoyo yosadetsedwa imene akristu ayenera kukhala. Malamulo ace ayenera kutsungidwa ngati tidzakhala ndi mabanja olimba ndi mipingo yolimba.

Tiyeni ti[illegible] cimene Buku Lopatulika linena kwa ife pokhud[illegible] ukhala wosa[illegible]sedwa.

**GAWO LOYAMBA:** (We[illegible]ngani Mateyu 19:4-6.)

Mulungu adapeleka ukwati monga kukhala pamodzi kodalitsidwa pakati pa mwamuna m'modzi ndi mkazi m'modzi. Mulungu adalenga mwamuna ndi mkazi. Anawapanga osiyana kuti pamodzi angakhale munthu m'modzi.

Ndi cifuniro ca Mulungu kuti munthu adzasiya atate ace ndi amai ace ndi kukwatira mkazi wace. Ndi cifuniro ca Mulungu kuti mwanayo ndi mkaziyo akhale thupi limodzi. Ukwati ndi ubale woyela. Mulungu afuna kuti tidzikonda ndi kulemekeza akazi athu kapenanso amuna athu.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Munthu ali yense ndi wofunika kwa Mulungu. Anakonda ali yense kwambiri kuti anatuma mwana wace kuti afere macimo a aliyense. Ifetu, tiyenera kukonda. Tiyenera kukonda mabanja athu, abwenzi athu, anansi athu ndi akristu anzathu, koma osati othawa. Tiyeneranso kukonda adani athu ndi amene ationonga ndi kutikhalika kuipa.

Tiyenera kuonetsa cikondi cathu mu zocita zathu, Buku Lopatulika likuti kwa ife, "...tisakonde ndi mau, kapena ndi lilime, komatu ndi kucita ndi m'coonadi." (1 Yohane 3:18).

PEMPHERO: Thokodzani Mulungu kamba ka cikondi cace cacikulu kwa anthu onse kuli konse. Pemphelerani cikondi ca Mulungu kuti cikhale mwa ife.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:13 |
| Laciwiri | Mateyu 25:40 |
| Lacitatu | Mateyu 5:21-22 |
| Lacinai | Luka 10:30-37 |
| Lacisanu | Luka 10:36-37 |
| Loweluka | Mateyu 22:39 |
| Lasabata | 1 Yohane 3:18 |



Amene anawaona anadziwa kuti cinthu cina cidacitika. Patsiku limodzi anthu zikwi adapulumutsidwa.

Mphamvu ya Mulungu ikalipo kwa ife lero. Tiyenera kulapa macimo athu ndi kusiya macimo athu ndi kudzipeleka kwa Mulungu. Tiyenela kufunsa Mzimu Woyera kuti utiziwise. Pambuyo pace tiyenela kuulola kuti utitsogolele nthawi yonse.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Tifuna cisitsimutso mdziko lathu lapansi lero. Tifuna citsisimutso mudziko lathu lino. Tifuna akristu amene amayikadi dzina la Mulungu ndi m'mene akhalira. Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pa cabe." (Eksodo 20:7).

Tiyeni tidzifunse ngati tikuswa lamuloli m'makhalidwe anthu.

PEMPHERO: Pempherani kuti mzimai ali yense adzazipeleka kwa Mulungu lero. Pempherani kuti Mulungu adzatuma citsitsimutso masiku ano.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:7 |
| Laciwili | Yesaya 6:3 |
| Lacitatu | Luka 6:46 |
| Lacinai | 1 Yohane 2:4-6 |
| Lacisanu | Yohane 14:15 |
| Loweluka | Mateyu 16:24 |
| Lasabata | Mateyu 16:25:26 |

PROGRAMU 5

COPHUNZIRA PAMIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KUTSUNGA TSIKU LA AMBUYE.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"Uzikumbukira tsiku la sabata likhale lopatulika."*

*Eksodo 20:8*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: (Welengani Eksodo 20:8-11).

Ndimezi zitiudza kuti Mulungu anapanga tsiku limodzi pa matsiku asanu ndi awiri kukhala lapadela. Adalidalitsa tsikuli ndi kuliika padera monga tsiku lopumila. Lamulo la cinai litiudza, "Uzikumbukira tsiku la sabata likhale lopatulika." (Eksodo 20:8)

Lero tidzaphunzira lamuloli.

GAWO LOYAMBA: Buku Lopatulika litiudza kuti Mulungu adalenga dziko pa matsiku asanu ndi limodzi. Pa tsiku la cisanu ndi ciwiri adapumula. Anaudza ana ace kuti adzicita nchito yao pa matsiku asanu ndi limodzi, koma tsiku la cisanu ndi ciwiri linkakhala tsiku lopumula.

Mulungu adalenga tsikuli kamba ka cikondi kwa ife. Adziwa cimene ndi cabwino pa ife. Adziwa kufuna kwathu kwa mtendere, cimwemwe ndi ciyanjano. Adziwa kufoka kwathu ndi kufuna kwathu kwa mphamvu. Motero Mulungu adaika padera tsiku limodzi mu sabata ili yonse monga tsiku loyera. Tsikuli linali ndi zolinga ziwili.

Coyamba, tsiku la Sabata linkakhala tsiku lopuma pa zinchito zathu. Linapatsidwa kwa ife monga tsiku limene tingapumile ndi kuthandidza mathupi athu ndi maganizo athu.



maganizo abwino ndi zolinganso zabwino. Cidano, mkwiyo ndi kulankhula zoipa zicokera kwa satana ndipo sidzingakondweretse Mulungu.

GAWO LACINAI: Njira ina m'mene sitingaphunzire lamulo la 'usaphe' ndi kutsasamalira anthu ena. (uku ndi kutsasamala). Yesu ananena nthano mu Luka 10:30-37 yokhudza munthu amene adamenyedwa ndi akawalala ndipo adatsiidwa kuti afe pa njira. Anthu awiri adabwera ndipo adamuona, koma padalibe amene adaima kuti amuthandidze. Anangopita mwamusanga ndi kumusiya kuti afe. Awa anali ndi mlandu monga amene adamumenya.

Munthu wina wacitatu adabwelapo pa malowo. Anamuona munthu womenyedwayo. Adaima mwa mtsanga kuti amuthandidze. Adasuka zilonda zace napita naye kumalo kumene ankayanganiridwa bwino. Adapeleka ndarama zace zomutsungira munthuyo.

Yesu adafunsa, "Uti wa awa atatu, uyesa iwe, anakhala m'nansi wa iye uja adagwa m'manja a acifwamba?" Yankho loona lidapelekedwa, "Iye wakumcitira cifundo." Yesu adati, "Pita, nucite iwe momwemo." (Luka 10:36, 37).

Yesu adaudza omutsatira ace kuti lamulo loyamba lalikuru ndi kukonda Mulungu. Pambuyo pace adati laciwiri ndi, "...Udzakonda muzako monga udzikonda iwe mwini." (Mateyu 22:39).

Tiyenela kulola Mulungu kuti acotse cidano, mkwiyo ndi kutsasamala m'miyoyo yathu, koma izi si zokwanira. Tiyeneranso kukhala ndi cikondi pa anthu ena cimene citipangitsa kuti tithandidze anthu osowa, kutsamalira obvutika, kutsangalitsa wosakondwa, kukhala ndi cikondi ca Kristu mwini wace. Cikondici ciyenera kudziwika m'njira imene tikhalira ndi anthu onse.

menyedwa kwambiri kuti anafa patapita matsiku ocepa. Atate ace adati "Ndinapha mwana wanga. Ngati sindinamuphunzitse kumwa mowa, ankakhala ndi moyo lero."

"...Cifukwa munacitira ici m'modzi wa abale anga, ngakhale ang'onong'ono awa, munandicitira ine." (Mateyu 25:40). Mauwa a Yesu ayenera kukhala m'mtima yathu. Adzatithandidza kukumbukira kuti sitingacite kanthu kuli konse pofuna kuononga munthu wina.

GAWO LACITATU: Yesu adalankhulapo pa za lamulo limene tiphunzira lero. Adati "Munamva kuti kunanendwa kwa iwo akale, usaphe; koma yense wakupha adzakhala wopalamula mlandu; koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wokwiyira mbale wace wopanda cifukwa adzakhala wopalamula mlandu; ndipo amene adzanena ndi mbale wace wopanda pace iye, adzakhala wopalamula mlandu wa ukuru; koma amene adzati, citsiru iwe: adzakhala wopalamula gehena wa moto." (Mateyu 5:21, 22).

Yesu akulankhula kuti maganizo athu ndi zolinga zathu zili zopambana kwambiri. Zocita zathu zicokera ku maganizo athu. Tsitiyenela kukhala wokalipa ndi m'bale wathu kapena wina aliyense cifukwa mkwiyo ndiye mbeu imene ingapitilire kukupha. Ngati munthu akalipa ndi munthu wina, caciwili ndi kuda munthuyo. Kuda kungabweletse kupha.

Tingaphe munthu osati popha thupi lace. Kumuitana kuti citsiru, kutanthaudza kuti kamunthu kosaziwika, ndi kumucita monga citsiru nthawi zonse, ndi kupha umuthu wace.

Tingaphe munthu poononga mbiri yace. Pamene ticita ukazitape kapena kukamba zonama zokhudza munthu wina tingaononge mbiri yace. Pamene tiononga mbiri ya munthu, tingamuononge kapena kumupangitsa kuti adzionongе.

Zinthu zimene tili nazo m'mitima yathu zitipangitsa kuti tidzicita m'mene ticitira. Akristu ayenela kukhala ndi mitima yoyela ndi



Caciwiri, tsiku la sabata linkakhala tsiku la mapemphero ndi lothokodzera. Linka khala tsiku loyera. Linapatsidwa kwa ife monga tsiku pamene tingapedzele cithandidzo pa zosowa zathu za thupi.

Tiyenela kuthokoza Mulungu potipatsa ife tsikuli la padela ndi loyera.

GAWO LACIWIRI: Ndime 9 itiudza kuti, "Masiku asanu ndi limodzi udzigwira ndi kumariza nchito zako zonse." Apa Mulungu atituma kuti tidzigwira nchito. Ici ndi cimodzi ca zifuniro za Mulungu pa ife.

Mulungu safuna kuti tikhale aulesi. Paulo atiudza m'cipangano catsopano "... ngati munthu safuna kugwira nchito, asadyetso." 2 Atesalonika 3:10

Analemba kwa akristu, kuwaudza "... ndi kugwira nchito ndi manja anu, monga tinakuuzani; kuti mukayende oona mtima pa iwo a kunja, ndi kukhala osasowa kanthu." (1 Atesalonika 4:11, 12). Nchito yonse yoona ndi yabwino ndipo ndi yokondweretsa kwa Mulungu. Pali matsiku asanu ndi limodzi amene tiyembekezedwa kugwira nchito kuti tingapedze zosowa zathu zathupi.

Pambuyo pace Mulungu akuti, "koma tsiku la cisanu ndi ciwiri ndilo sabata la Yehova Mulungu wako usagwire nchito iri yonse .." (Eksodo 20:10). Mulungu anafuna kuti tikhale na tsiku lopumila. Sanafuna kuti tidzikhala cabe nthawi zonse.

Nchito zina zingacitidwe angakhale pa tsiku la sabata. M'nyumba zathu tiyenera kuphika cakudya ndi kuyang'anira mabanja anthu. Anthu ena, monga ma dotoro ndi masisita, ali ndi nchito zimene ayenera kugwira ndi pa sabata pomwe. Mulungu amvera cimeneci.

Koma, tiyenera kutsunga sabata monga tsiku loti mathupi athu apume. Ngati tigwira nchito pa tsikuli tiyenera kukumbukira kuti Mulungu afuna kuti tipume.

GAWO LACITATU: M'nthawi yam'cipangano cakale, tsiku la sabata linali la cisanu ndi cimodzi. Ayuda amene sanakhulupirire mwa Yesu akali kusunga tsiku la cisanu ndi cimodzi monga sabata.

Yesu anauka kwa akufa pa tsiku loyamba, la sabata. Atapita ku mwamba, akristu adayamba kukomana pa sabata m'malo mwa pa ciwelu. Anayamba kuitana sabata "Tsiku la Ambuye."

Akristu apitirira kukomana kuti apemphere pa tsiku la Ambuye, sabata. Mulungu anatiudza kusunga tsikuli kukhala loyela. Liyenela kukhala tsiku la mapemphero ndi lothokodzera Mulungu. Tiyenela kukhala okhulupirika popita ku machalichi kwathu.

Anthu ena lero akuti angapembedze Mulungu kulikonse. Aganidza kuti chalichi salifuna. Mlembi wa Ahebri anaudza akristu aci Hebri kuti atsasiye kukomana pamodzi pofuna kupemphera. (Welengani Ahebri 10:25).

GAWO LACINAI: Kodi akristu ayenela kucita ciani dzuwa lonse la sabata? Pa nthawi ya cipangano catsopano Ayuda anali ndi malamulo ambiri osungila sabata. Panali zinthu zopitilira chikwi cimodzi zimene sankatha kucita pa tsiku la sabata. Nthawi zonse ankafuna kuona kuti aliyense anali kutsunga malamulowa. Amene sanasunge malamulo a sabata anali kulangidwa koposa.

Pamene Yesu adabwera, anadzuzula njirayi yotsungira tsiku la sabata. Tsiku limodzi la sabata Yesu ndi ophunzira ace anali kuyenda m'minda. Anali ndi njala ndipo adatengako zakudya m'munda. Afarisi adati, "...Taona acitiranji cosaloleka kucitika patsiku la sabata?" (Marko 2:24).



kupha m'nzace. Ici cingakhale cifukwa ca nsanje kapena cidano. Angaganidzire za zimenezo ndi kuyamba kupanga mapulani omuphera muzace.

Nthawi zina pali kupha kosakonzekera. Ici cingacitike pamene anthu amenyana. Nthawi zambiri cicitidwa ngati munthu aledzela ndipo akalipisidwa kamba ka kanthu kina. Kumwa mowa kutsogozela ku kupha.

Nthawi zina makolo angamenye mwana mokalipa ndi kumupha mwanayo osafuna kuti amuphe. Nthawi zina mkazi angafune kupha mwana wasabadwa amene samufuna. Nthawi zina munthu angaziphe yekha.

Kupha kuli konse kwa munthu amene adalengedwa ndi Mulungu ndi koipa. Pamene moyo wa munthu uonongedwa, ucimo ucitika kwa Mulungu.

GAWO LACIWIRI: Sitiyenera kucita kanthu kali konse kamene kadzabweretsa imfa kwa munthu wina. Tiyeni tiwelenge mau a Mulungu. (Welengani Mateyu 25:35-45.) Yesu akutiudza mu ndimezi kuti pamene ticita zinthu ndi anthu ena ticita ndi Mulungu. Zimene ticita kwa anthu ena, ticita kwa Mulungu.

Tiyenela kukhala otsamala kuti sitisogodza munthu kucita cinthu cimene cidzamutengera moyo wace. Tiyenera kukhala osamala kwambiri kuti tikhala miyoyo yolungama. Sitiyenela kutsogoza mbale wathu wofoka ku mayesero ndi ucimo.

Munthu wina adali ndi mwana wace wa mwamuna amene adamukonda. Sankaganizira zomupha mwanayo. Koma, munthuyo anaganidza kuti ndi cabwino kumwa mowa. Sankaledzela ndipo ankaumvera bwino mowawo. Mwanayo anayamba kumwa mowa ku nyumba ndi atate ace. Anali ndi nthawi yabwino.

Koma tsiku lina mwanayu anapita kwina kukamwa ndi anzace. Anayamba kumenyana. Ana-

PRGRAMU 7

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KULEMEKEDZEDWA KWA MOYO WA MUNTHU.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:
*"Usaphe."*

*Eksodo 20:13*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Lamulo la Mulungu limene tidzaphunzira lero litiudza kuti titsatenge moyo wa munthu wina. Tingaganidzire kuti sitifuna kuudzidwa kuti tisaphe. Azimai acikristu sangaganizire zopha munthu.

Kapena ici ndi coona. Koma, kupha sikuyamba monga kupha. Kuyamba ndi nsanje kapena cidano, kapena kufuna kuti munthu masiku onse azikhala oyamba. Kumayamba m'mtima mwa munthu.

Buku Lopatulika litiuzanso kuti pali njira zophera munthu osati kumupha cabe thupi lace. Tidzaphunzira tanthauzo la lamuloli lero.

GAWO LOYAMBA: Lamulo lakuti "Usaphe," silitanthauza kuti tisaphe nyama, mbalame kapena nsomba kuti tidye. Buku Lopatulika linena zopha munthu, amene ali ndi mzimu umene udzakhala kwa muyaya. Nyama zilibe mizimu.

Palibe munthu amene ali ndi udindo wophera munthu m'nzace. Moyo ucokera kwa Mulungu. Ndi Mulungu yekha amene angapeleke moyo. Munthu anapangidwa mcifanizo ca Mulungu. Munthu ali ndi mzimu. Ngati munthu akupha munthu m'nzace akuononga moyo umene Mulungu adapeleka. Tiuzidwa poyera mu mau a Mulungu kuti sitiyenera kuononga moyo.

Kupha ndi kosiyana. Nthawi zina kamba ka maganizo oipa m'mtima, munthu aganizira



Yesu adawaudza, "sabata linaikidwa cifukwa ca munthu, simunthu cifukwa ca sabata; motero mwana wa munthu ali mwini dzuwa la sabata lomwe." (Marko 2:27, 28.)

Yesu anali kuwaudza kuti tsiku la sabata linapatsidwira ife. Sitifuna malamulo ambiri kuti tisunge tsiku la Ambuye. Tiyenera kuwelenga mau a Mulungu, kulankhula naye, kupemphera pamodzi ndi akristu ena. Tipumitse mathupi athu ndi maganizo athu.

Tisacite zinthu zimene sidzidzabweletsa ulemu kwa Mulungu. Ngati kristu ndi Ambuye wa miyoyo yathu yonse, adzakhala Ambuye a sabata wathu.

MTSOGOLERI WAPUROGIRAMU: Pa mwezi wasilawu takhala tili kuphunzira malamulo anai. Onse akhudza ubale wathu ndi Mulungu. Taphunzira kuti Mulungu afuna kukhala oyamba pa miyoyo yathu. Atiudza kuti tisalambire mafano, ndiponso usachule dzina lace pacabe. Tiyenela kusunga tsiku lace, la sabata, kukhala lopatulika. Akristu ayenera kusunga malamulowa cifukwa ca cikondi cao ndi Mulungu. Taphunzira kuti Yesu adati lamulo lalikulu ndi kukonda Mulungu ndi mitima yathu yonse, ndi miyoyo yathu yonse, ndi nzeru zathu zonse. (Mateyu 22:37). Ngati ticita cimeneci, tidzamvera malamulo amene takhala tili kuphunzira.

PEMPHERO: Pempherani kuti tikonde Mulungu koposa zinthu zina zonse pa miyoyo yathu.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9.

ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:8 |
| Laciwiri | 2 Atesalonika 3:10 |
| Lacitatu | 1 Atesalonika 4:11-12 |
| Lacinai | Eksodo 20:10 |

| | |
|---|---|
| Lacisanu | Ahebri 10:25 |
| Loweluka | Marko 2:27-28 |
| Lasabata | Mateyu 22:37 |



ZOWELENGA M'BUKU LOPATULIKA SABATA LINO

| | |
|---|---|
| Lolemba | Eksodo 20:12 |
| Laciwiri | Mateyu 22:37 |
| Lacitatu | Aefeso 6:1 |
| Lacinai | Akolose 3:20 |
| Lacisanu | Aefeso 6:4 |
| Loweluka | Miyambo 1:8 |
| Lasabata | Miyambo 4:1 |

coona. Makolo acikristu ayenera kufunsa Mulungu kuti awatsogodze. Mu tauni ili yonse muli zipatala zothandidza poganizira kuculuka kwa ana munthu angakhale nao. Makolo acikristu asaope kulankhula ndi anthuwa kapena kwa dotoro kapena kufunsa thandizo pa banja lao.

Makolo a cikristu ayenera kukhala omvera ndipo anzeru. Sayenela kukonda mwana m'modzi koposa wina. Sayenera kukhala a umbombo ndipo ayenera kukhala okhulupirika. Ayenera kukhala okhulupirika m'zinthu zonse. Ayenera kuona kuti zilango zawo ziliko bwino.

Makolo ayenera kuika Mulungu poyamba pa miyoyo yao m'nyumba zao. Kopanda Mulungu sitingaphunzitse bwino ana munjira zabwino. Tifuna Mzimu Woyera kuti utisogolere ndi kutipatsa mphamvu ndi nzeru. Ngati ana aonadi Yesu pa miyoyo yathu matsiku onse, adzakhala okondwa kumvera ndi kulemekeza makolo ao.

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Tiyeni tiganidzire kwambiri za mabanja athu. Kodi muli mukangano? Kodi muli sanje? Kodi muli cisokonezo, mkwiyo, kapena cidano?

Kapena muli cikondi, kulemekedzana, kumvera, ndi kukhulupirirana? Muli cikondi ca Mulungu, mtendere ndi cimwemwe?

Tonse tifuna kukhala ndi mabanja okondwa acikristu. Tiyeni tidzipeleke kwa Mulungu kuti tikhale azimai amene Mulungu afuna kuti tikhale. Tiyeni tipempherere usogoleri wace ndi nzeru zace. Tiyeni tifune-fune cifuno cace mzonse zimene ticita.

PEMPHERO: Pempherani kuti tiphunzitse ana athu njra za Mulungu. Pempherani kuti tikhale makolo amene Mulungu afuna.

NYIMBO YA AZIMAI: 1 Akorinto 3:9.



PROGRAMU 6

COPHUNZIRA PA MIYEZI ITATU: MALAMULO KHUMI NDI MKRISTU LERO.

COPHUNZIRA LERO: KULEMEKEDZA MAKOLO.

NTHAWI YA PEMPHERO:

MAU A PAMTIMA:

*"Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti acuruke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe."*

*Eksodo 20:12*

MTSOGOLERI WA PROGRAMU: Taphunzira malamulo oyamba anai amene anena za ubale wathu ndi Mulungu. Yesu anatiudza njira yomverera malamulowa: "...Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse." (Mateyu 22:37).

Malamulo asanu ndi limodzi m'malamulo khumi alankhula kwa ife za ubale wathu ndi anthu ena. Buku Lopatulika lilankhula poyamba za ubale wofunika kwambiri pakati pa makolo ndi ana. Mau athu a pamtima atiudza "Uzilemekeza atate wako ndi amako, kuti acuruke masiku ako mdziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe." (Eksodo 20:12).

Lero tidzaphunzira tanthaudzo la lamuloli.

GAWO LOYAMBA: Lamuloli lili ndi lonjezo kwa anthu amulungu. Litiudza kuti ngati tilemekedza makolo athu matsiku athu adzaculuka mdziko limene Ambuye atipatsa ife. Mulungu anali kulankhula kwa ana a Israyeli. Anali kuwaonetsa njira yopangira mtundu wolimba ndi kupitilidza kucita ubwino mdziko lomwe Mulungu adawapatsa iwo.

Banja limene ana akonda, alemekeza ndi kumvera makolo awo lidzakhala banja lolimba. Dziko liyenela kukhala ndi mabanja olimba kuti likhale dziko lamphamvu. M'dziko liri lonse

mabyuto amabwera ngati mabanja ali ofika. Pamene ana sakonda ndi kulemekeza ndi kumvera makolo awo m'nyumba mwao simudzakhala ulemu ndi makhalidwe abwino m'dziko.

Conco, tingaone kufunika kwace kokhalira ndi mabanja olimba. Makolo ayenera kuphunzitsa ana ao kulemekedza atate ao ndi amao. Pambuyo pace tidzakhala ndi mabanja olimba ndiponso dziko lamphamvunso.

GAWO LACIWIRI: M'malo ena atate amapasidwa ulemu wapadera, osati amai. Mulungu atiudza kulemekeza onse atate ndi amai. Atate ndiye mtsogoleri wa banja la cikristu, koma mai nayenso ayenera kulemekedzedwa, ndi kumveledwa ndi ana.

M'mabanja ambiri matsiku ano ana samvera makolo ao. Ici ndi coipa kwambiri. Tiudziwa mu Aefeso 6:1. "Ananu, mverani akukukbalani mwa Ambuye, pakuti ici ndi cabwino." Ndiponso mu Akolose 3:20 tiwelenga, "Ana inu, mverani akubala inu m'zonse, pakuti ici Ambuye akondwera naco."

Makolo adziwa koposa ana. M'zaka zimene akhala pansi pano aphunzira zinthu zambiri. Angakhale kuti ana ali ophunzira bwino koposa makolo ao, pali zinthu zina zambiri za pa moyo zimene makolo adziwa kamba ka matsiku amene akhala mdziko.

Makolo ayenera kuphunzitsa ana ao njila yabwino yokhalira. Ayenera kuona kuti ana ao awamvera iwo. Mulungu adapanga kuti makolo ayenera kukhala olamulira m'nyumba kuti angaphunzitse ndi kutsogoza ana ao m'njira yabwino.

Makolo acikristu adzayanjana kwa Mulungu kuti apeze nzeru. Adzatsogodza ana ao kuti akonde Mulungu ndi kumutsatira m'zonse zimene acita.

GAWO LACITATU: Nthawi zina ana amakana ku makolo awo. Safuna kuudzidwa cocita. Nthawi



zina akana kumvera. Angakhale mwana wa m'ng'ono angayang'ane amai ace ndi kunena "toto," pamene awudzidwa kucita cinthu cina.

Kumvera ndi kwabwino. Ali yense ayenera kuphunzira kumvera. Mwana amene acita zimene afuna nthawi zonse sadzakhala mwana wokondwa. Ngati ndi kofunika, makolo ayenera kuwalanga ana ao kuti adzimvera.

Ngati mwana wanu ndi wodwela, mumuumilidza kuti amwe mankwala amene adotolo apeleka, angakhale kuti sayafuna. Mucita ici cifukwa mdziwa kuti adzamukhazika bwino. Ngati mwana wanu afuna kusewela pafupi ndi msinje, m'mucotsako angakhale kuti safuna kuti acotsedwe. Ngati mwana wanu adayamba kumwa parafini, munkamulesa msanga, angakhale kuti ankalila.

Sitilola kuti ana athu acite zinthu zimene zinkawapweteka. Sitiyenela kuwalola kuti adzicita zinthu m'njira iri yonse. Tisamawalola kuti azinka njira yao pamene tiziwa kuti sindiyo yenera.

Ngati ana athu alakwa tiyenela kuwaudza kuti zimene acita ndi zolakwa ndi kuwalanganso kuti atsazacitenso. Ana ena amakuwa ndi kuyambana pofuna kucita zimene afuna. Anawo adzakula kukhala anthu akulu amene pocita zinthu nthawi zonse ndi kukangana. M'nyumba zathu tiyenela kuwaphunzitsa ana athu kumvera, ndipo tiyenela kuwalanga ngati samvera.

Makolo ayenera kukhala m'njira yoti ana adzakondwera. Makolo ayenera kukhala ndi cikondi coonadi pa ana ao. Ayenera kuonetsa cikondici kwa ana ao. Pali ana ambiri mdziko lapansi amene adziwa kuti sakondedwa kapena safunidwa. Makolo aci Kristu ayenela kukonda ana ao.

Nthawi zina makolo amakhala ndi ana ambiri. Amatopa kwambiri. Palibe ndalama zokwanira kugula zobvala ndi fizi ndi zinthu zina zofunika. Ndi kobvuta kuonetsa cikondi